Imbani Nyimbo Yothandiza Kukhala Olimba Mtima

Werengani Salimo 27:6. Davide ankakonda kuimba ndipo nthawi zambiri ankaimba nyimbo zotamanda Yehova. Nyimbo zambiri zimene ankaimbazo zinamuthandiza kuti akhale wolimba mtima. Nanunso kuimba kungakuthandizeni kuti mukhale olimba mtima.

Werengani mawu a nyimbo yakuti, "Tithandizeni Kukhala Olimba Mtima." Kodi m'nyimboyi muli mfundo ziti zimene zikusonyeza chifukwa chake tiyenera kukhala olimba mtima? Lowezani nyimboyi ndipo muimbe limodzi ndi banja lanu.

PINDANI

NYIMBO 137

Tithandizeni Kukhala Olimba Mtima

(Machitidwe 4:29)

1. Polalikira Ufumu,
Kukweza dzina lanu.
Anthu ena amatsutsa,
Ndiponso kutinyoza.
Koma sitiwaopa
Timamvera inu nokha.
Choncho Yehova, tikupempha
Mutipatse mzimu wanu.

(KOLASI)

Polalikira uthenga,
Mutichotsere mantha.
Tikhale olimba mtima
Anthu amve uthenga.
Amagedo ikufika,
Tikhale olimba mtima,
Tithandizeni Yehova.
Tikupempha.

2. Pamene tichita mantha,
Mudziwa ndife fumbi.
Mudzatithandiza ndithu
Paja munalonjeza.
Imvani kuopseza,
Kwa anthu odana nafe.
Tithandizeni, tisaope.
Tikhale olimba mtima.

(KOLASI)

www.jw.org/ny © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania